

NYANJA (CHICHEWA)	NEW INTERNATIONAL VERSION
TITUS 1	TITUS 1
Tit 1:1 Paulo, mtumiki wa Mulungu, ndi mtumwi wa Yesu Khristu, monga mwa chikhulupiriro cha wosankhika a Mulungu, ndi chizindikiritso cha chowonadi chiri monga mwa chipembedzo.	1 Paul, a servant of God and an apostle of Jesus Christ for the faith of God's elect and the knowledge of the truth that leads to godliness—
Tit 1:2 M'chiyembekezo cha moyo wosatha, umene Mulungu, wosanamayo, adalonjeza lisadakhale dziko lapansi;	2 a faith and knowledge resting on the hope of eternal life, which God, who does not lie, promised before the beginning of time,
Tit 1:3 Koma panyengo za lye yekha adawonetsa mawu ake mu ulalikiro, umene adandisungitsa ine, monga mwa lamulo la Mpulumutsi wathu Mulungu;	3 and at his appointed season he brought his word to light through the preaching entrusted to me by the command of God our Savior,
Tit 1:4 Kwa Tito mwana wanga weni weni monga mwa chikhulupiriro cha ife tonse; chisomo, chifundo ndi mtendere za kwa Mulungu Atate ndi Ambuye Yesu Khristu Mpulumutsi wathu.	4 To Titus, my true son in our common faith: Grace and peace from God the Father and Christ Jesus our Savior.
Tit 1:5 Chifukwa cha ichi ndidakusiya iwe mu Krete, kuti ukalongosole zosowa, nukayike akulu m'mizinda yonse, monga ndidakulamulira:	5 The reason I left you in Crete was that you might straighten out what was left unfinished and appoint[a] elders in every town, as I directed you.
Tit 1:6 Ngati wina ali wopanda chilema, mwamuna wamkazi m'modzi, wokhala nawo ana wokhulupirira, wosakaza zake, kapena wosakana kumvera mawu.	6 An elder must be blameless, the husband of but one wife, a man whose children believe and are not open to the charge of being wild and disobedient.
Tit 1:7 Pakuti woyang'anira ayenera kukhala wopanda chilema, ngati mdindo wa Mulungu; wosati waliwuma, wosapsa mtima msanga, wosamwetsa vinyo, wosati wa chiwawa, wopanda ndewu, wosati wa chisiliro chonyansa.	7 Since an overseer[b] is entrusted with God's work, he must be blameless—not overbearing, not quick-tempered, not given to drunkenness, not violent, not pursuing dishonest gain.
Tit 1:8 Komatu wokonda kuchereza alendo, wokonda anthu abwino, wosaledzera wolungama, woyera mtima, wodziletsa;	8 Rather he must be hospitable, one who loves what is good, who is self-controlled, upright, holy and disciplined.
Tit 1:9 Wogwira mawu wokhulupirika monga mwa chiphunzitso, kuti akakhoze kuchenjeza m'chiphunzitso cholamitsa, ndi kutsutsa wotsutsana naye.	9 He must hold firmly to the trustworthy message as it has been taught, so that he can encourage others by sound doctrine and refute those who oppose it.
Tit 1:10 Pakuti alipo ambiri wosamvera mawu, woyankhula zopanda pake, ndi wonyenga maka maka iwo a kumdulidwe:	10 For there are many rebellious people, mere talkers and deceivers, especially those of the circumcision group.

NYANJA (CHICHEWA)	NEW INTERNATIONAL VERSION
Tit 1:11 Amene ayenera kutsekedwa pakamwa; ndiwo amene apasula mabanja, ndi kuphunzitsa zosayenera chifukwa cha chisiliro chonyansa.	11 They must be silenced, because they are ruining whole households by teaching things they ought not to teach—and that for the sake of dishonest gain.
Tit 1:12 Wina wa mwa iwo, ndiye m'neneri wa iwo wokha, adati, Akrete ndiwo abodza masiku onse, zirombo zoyipa, aulesi ndi adyera.	12 Even one of their own prophets has said, "Cretans are always liars, evil brutes, lazy gluttons."
Tit 1:13 Umboni uwu uli wowona. Mwa ichi uwadzudzule mokalipa, kuti akakhale wolama m'chikhulupiro.	13 This testimony is true. Therefore, rebuke them sharply, so that they will be sound in the faith
Tit 1:14 Osasamala nthano zachabe za chiyuda, ndi malamulo wa anthu wopatuka kusiyana nacho chowonadi.	14 and will pay no attention to Jewish myths or to the commands of those who reject the truth.
Tit 1:15 Kwa oyera mtima zonse ndi zoyera: koma mwa iwo wodetsedwa ndi wosakhulupira kulibe kanthu koyera; komatu zadetsedwa nzeru zawo ndi chikumbumtima chawo.	15 To the pure, all things are pure, but to those who are corrupted and do not believe, nothing is pure. In fact, both their minds and consciences are corrupted.
Tit 1:16 Abvomereza kuti adziwa Mulungu, koma ndi ntchito zawo amkana Iye, popeza ali wonyansitsa, ndi wosamvera, ndi pa ntchito zonse zabwino wosatsimikizidwa.	16 They claim to know God, but by their actions they deny him. They are detestable, disobedient and unfit for doing anything good.
TITUS 2	TITUS 2
Tit 2:1 Koma iwe, yankhula zimene ziyenera chiphunzitso cholamitsa:	1 You must teach what is in accord with sound doctrine.
Tit 2:2 Wokalamba akhale wodzisunga, wolemekezeka, wodziletsa, wolama m'chikhulupiro, m'chikondi, m'chipiliro. Free Bibles: http://freebiblegospeltoallnations.blogspot.com 292 Chewa Holy Bible - New Testament	2 Teach the older men to be temperate, worthy of respect, self-controlled, and sound in faith, in love and in endurance.
Tit 2:3 Momwemonso akazi wokalamba akhale nawo makhalidwe woyenera anthu woyera, wosasinjirira, wosamwetsa vinyo, akuphunzitsa zinthu zokoma.	3 Likewise, teach the older women to be reverent in the way they live, not to be slanderers or addicted to much wine, but to teach what is good.
Tit 2:4 Kuti akalangize akazi ang'ono kuti akhale wodziletsa akonde amuna awo, akonde ana awo, anzeru wosati achiwerewere.	4 Then they can train the younger women to love their husbands and children,
Tit 2:5 Akhale wosunga nyumba abwino, akumvera amuna a iwo okha, kuti mawu a Mulungu angachitidwe mwano.	5 to be self-controlled and pure, to be busy at home, to be kind, and to be subject to their husbands, so that no one will malign the word of God.
Tit 2:6 Momwemonso anyamata uwadandaulire akhale wodziletsa.	6 Similarly, encourage the young men to be self-controlled.

NYANJA (CHICHEWA)	NEW INTERNATIONAL VERSION
Tit 2:7 Mzinthu zonse udziwonetsere wekha chitsanzo cha ntchito za bwino; m`chiphunzitso chako uwonetsere chosabvunda, ulemekezeko, ndi ulemu.	7 In everything set them an example by doing what is good. In your teaching show integrity, seriousness
Tit 2:8 Mawu olama, wosatsutsika; kuti iye wakutsutsana nawe achite manyazi, posakhala nako kanthu koyipa kunenera inu.	8 and soundness of speech that cannot be condemned, so that those who oppose you may be ashamed because they have nothing bad to say about us.
Tit 2:9 Uwalimbikitse akapolo amvere ambuye wawo wa iwo wokha, nawakondweretse m`zinthu zonse; wosawiringula mawu awo;	9 Teach slaves to be subject to their masters in everything, to try to please them, not to talk back to them,
Tit 2:10 Akhale wosaba, koma awonetsere kukhulupirika konse kwa bwino: kuti akakometsere chiphunzitso cha Mulungu Mpulumutsi wathu mzinthu zonse.	10 and not to steal from them, but to show that they can be fully trusted, so that in every way they will make the teaching about God our Savior attractive.
Tit 2:11 Pakuti chisomo cha Mulungu chimene chibweretsa chipulumutso chawonekera kwa anthu onse,	11 For the grace of God that brings salvation has appeared to all men.
Tit 2:12 Ndikutiphunzitsa ife kuti, pokana chisapembedzo ndi zilakolako za dziko lapansi, tikhale ndi moyo mdziko lino wodziletsa, ndi wolungama, ndi wopembedza;	12 It teaches us to say "No" to ungodliness and worldly passions, and to live self-controlled, upright and godly lives in this present age,
Tit 2:13 Akulindirira chiyembekezo chodala, ndi maonekedwe a ulemerero wa Mulungu wamkulu ndi Mpulumutsi wathu Khristu Yesu:	13 while we wait for the blessed hope—the glorious appearing of our great God and Savior, Jesus Christ,
Tit 2:14 Amene anadzipereka yekha m`malo mwa ife, kuti akatiwombole ife ku zoipa zonse, nakadziyeretsere yekha anthu akhale ake apaderadera achangu pa ntchito zabwino.	14 who gave himself for us to redeem us from all wickedness and to purify for himself a people that are his very own, eager to do what is good.
Tit 2:15 Izi yankhula, ndipo uchenjeze, nudzudzule ndi ulamuliro wonse. Munthu asakupeputse iwe.	15 These, then, are the things you should teach. Encourage and rebuke with all authority. Do not let anyone despise you.
TITUS 3	TITUS 3
Tit 3:1 Uwakumbutse iwo agonje kwa akulu, ndi aulamuliro awamvere woweruza ndi kukhala okonzeka ku ntchito iliyonse yabwino,	1 Remind the people to be subject to rulers and authorities, to be obedient, to be ready to do whatever is good,
Tit 3:2 Asachitire mwano munthu aliyense, asakhale andewu, akhale odekha, nawonetsere chifatso chonse pa anthu onse.	2 to slander no one, to be peaceable and considerate, and to show true humility toward all men.

NYANJA (CHICHEWA)	NEW INTERNATIONAL VERSION
Tit 3:3 Pakuti kale ifenso tidali opusa, osamvera, wonyengeka, akuchitira ukapolo zilakolako ndi zokondweretsa za mitundu mitundu, wokhala m`dumbo, ndi njiru, wodanidwa, wodana wina ndi mzake.	3 At one time we too were foolish, disobedient, deceived and enslaved by all kinds of passions and pleasures. We lived in malice and envy, being hated and hating one another.
Tit 3:4 Koma zitapita izo kukoma mtima, ndi chikondi cha Mulungu Mpulumutsi wathu chidawonekera kwa anthu.	4 But when the kindness and love of God our Savior appeared,
Tit 3:5 Zosati zochokera m`ntchito za m`chilungamo, zimene tidazichita ife, komatu monga mwa chifundo chake adatipulumutsa ife, mwakutsuka kwa kubadwanso ndi makonzedwe atsopano a Mzimu Woyera:	5 he saved us, not because of righteous things we had done, but because of his mercy. He saved us through the washing of rebirth and renewal by the Holy Spirit,
Tit 3:6 Amene adatsanulira pa ife mochulukira, mwa Yesu Khristu Mpulumutsi wathu:	6 whom he poured out on us generously through Jesus Christ our Savior,
Tit 3:7 Kuti poyesedwa wolungama ndi chisomo cha Iyetu, tikayesedwe wolowa nyumba monga mwa chiyembekezo cha moyo wosatha.	7 so that, having been justified by his grace, we might become heirs having the hope of eternal life.
Tit 3:8 Wokhulupirika mawuwa, ndipo za izi ndifuna ulimbitse mawu kuti iwo akukhulupirira Mulungu asamalire akhalebe atsogoleri antchito za bwino. Izi ndi zokoma ndi zopindulitsa anthu.	8 This is a trustworthy saying. And I want you to stress these things, so that those who have trusted in God may be careful to devote themselves to doing what is good. These things are excellent and profitable for everyone.
Tit 3:9 Koma pewa mafunso opusa ndi mawerengedwe amibado ndi ndewu, ndi makani apamalamulo; pakuti sizipindulitsa, ndipo zili zachabe.	9 But avoid foolish controversies and genealogies and arguments and quarrels about the law, because these are unprofitable and useless.
Tit 3:10 Munthu wopatukira chikhulupiriro, utamchenjeza kamodzi ndi kawiri, umkanize;	10 Warn a divisive person once, and then warn him a second time. After that, have nothing to do with him.
Tit 3:11 Podziwa kuti wotereyo wasandulika konse, nachimwa, nakhala wodzitsutsa yekha.	11 You may be sure that such a man is warped and sinful; he is self-condemned.
Tit 3:12 Pamene ndituma Artema kwa iwe, kapena Tukiko, chita changu kudza kwa ine ku Nikopoli: pakuti ndatsimikiza mtima kugonerako kumeneko nyengo yozizira.	12 As soon as I send Artemas or Tychicus to you, do your best to come to me at Nicopolis, because I have decided to winter there.
Tit 3:13 Bweretsani Zena woyimirra milandu ndi Apolo mwachangu. Akonzereni za ulendo, kuti asasowe kanthu.	13 Do everything you can to help Zenas the lawyer and Apollos on their way and see that they have everything they need.
Tit 3:14 Ndipo anthu athu aphunzirensa kusunga ntchito zabwino zofunika, kuti asakhale wosabala zipatso.	14 Our people must learn to devote themselves to doing what is good, in order that they may provide for daily necessities and not live unproductive lives.

NYANJA (CHICHEWA)	NEW INTERNATIONAL VERSION
Tit 3:15 Akupatsani moni iwo wonse ali ndi ine. Apatseni moni	15 Everyone with me sends you greetings. Greet those who love us in the faith. Grace be with you all.